# CHIDZIWITSO

## KUTSEKEDWA KWA MILATHO YONGOYEMBEKEZERA YOYENDAPO MAGALIMOTO KOMANSO ANTHU PA MTSINJE WA LILONGWE

A Roads Authority akudziwitsa anthu onse za kutsekedwa kwa milatho imene imagwilitsidwa ntchito pa Mtsinje wa Lilongwe pa nthawi imene mlatho watsopano umamangidwa. Izi zili chonchi chifukwa cha kumaliza kumanga mlatho watsopano umene utsegulidwe pa 6 November 2025 kuti anthu oyenda pa mseu adzigwilitsa ntchito.

Ma Boma a Malawi ndi Japan kudzera ku Japan International Cooperation Agency (JICA), adasayinilana mgwirizano wa ndalama umene zina zomwe adagwirizana ndi kuchotsa milatho yongoyembekezerayi, komanso kubweza malo onse amene anabwerekedwa (temporary lease) kwa anu ake malowo, ntchito yomanga mlatho watsopano ikatha.

Pofuna kuchepetsa mavuto a kayendedwe pa nthawi imene mlatho watsopanowu umamangidwa, kampane imene imamanga mlathowu ya DAI NIPPON inajambula (design) ndi kumanga milatho yoyembekezera iwiri, wina woyendapo anthu ndi wina woyendapo magalimoto. Milatho imeneyi inamangidwa kuti igwiritsidwe ntchito mu nthawi imene mlatho watsopanowu umamangidwa, kuchokera m'mwezi wa November 2023 mpaka November 2025. Milatho yongoyembekezerayi sikuyenera kugwiritsa ntchito nthawi yayitali kapena kwa muyaya.

Ngati mbali imodzi yotsatira zoyenereza za mamangidwe komanso mgwirizano umene maiko awiriwa anapanga, ndikoyenera kuti milatho yongoyembekezerayi ichotsedwe ndipo izi zikutsatira ndondomeko ya ntchito zomangamanga komanso pofuna kuteteza miyoyo ya anthu motere:

1. Maziko ndi zina zokhudzana ndi milathoyi zinakonzedwa kuti zigwire ntchito nthawi yochepa kotero kuti kugwiritsa ntchito nthawi yayitali kungaike miyoyo ya anthu pa chiopsezo.
2. Malo amene panamangidwa mlatho wodutsa magalimoto komanso pamene kampane yomanga imagwirira ntchito zake, adabwerekedwa kudzera mu mgwirizano ndi anu ake malo (temporary lease). Kotero kuti malo amenewa akonzedwa ndi kubwezedwa kwa anu ake malowo monga mwa mgwirizano.

Oyenda pa mseu akupemphedwa kuti ayambe kugwiritsa ntchito moyenerera mlatho ndi mseu watsopano zimene zamangidwa mwa ukadaulo komanso zimene ziri zokhazikika ndi zotetezeka.

**Eng. Ammiel Champiti PhD**
**Chief Executive Officer**
**Roads Authority**
**Date:** 6th November 2025